

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

MPHAMVU YA MAFANIZO

“Chifukwa chimenechi yense amene akamva mau anga amenewa, ndi kuwachita, ndidzamfanizira iye ndi munthu wochenjera, amene anamanga nyumba yake pathanthwe” (Mateyu 7:24). Pofanizira zinthu, Yesu, mwana wa Mulungu, anayamba kunena kwa khamulo za mkani imene inali yophweka komanso imene onse akanatha kuimvetsa mosavuta. Wodzozedwayo analibe maphunziro ozama a ukadaulo kapenanso sanapite ku sukulu yokaphunzira kalankhulidwe kozama, komabe Iye anadabwitsa anthu ndi nkhani zokhudza moyo wao wa tsiku ndi tsiku zimene zinawaunikira omverawo choonadi chauzimu. Nkhani zimenezi zinawiritisa malingaliro awo ndipo zinatakasa mzimu, kaganizidwe ndi nzeru zawo. Pamene Yesu amamaliza kunena nkhani ya munthu wochenjera ndi wina wopusa, “anthu anazizwa ndi chiphunzitsa chake: pakuti anawaphunzitsa monga mwini mphamvu, wosanga alembi” (28-29).

Nkhani zambiri zosavuta kumva komanso zokumbukirika zimene Yesu anazinena zimatchedwa mafanizo. Fanizo ndi chinthu chonenedwa mofananitsa, kapena nkhani yokhudza zochitika m'moyo wa tsiku ndi tsiku imene imatisiyira phunziro, mbiri yabwino kapena chakuti tichite. Mau akuti fanizo mu chiGriki ndiwo “kuika chinthu pambali... kumene kutanthauza kuika chinthu pambali pa chinzake ndi cholinga chofanizira” (*Vine's Expository Dictionary*). Komanso *Thayer's Greek Definitions* imanena kuti: “Fanizo ndi nkhani ya pansi pano koma yokhala ndi tanthauzo la chinthu chakumwamba.” Kumeneku ndiko kufanizira zinthu kapena nkhani yofanana imene yatengedwa ku chilengedwe kapena ku zochitika pakati pa anthu ndi cholinga chofuna kupeza phunziro lauzimu. Yesu anagwiritsa ntchito zifanifani ndi nkhani zimene zinali zofanana ndi chikhalidwe cha anthu aku derako panthawiyo. Yesu anaphunzitsa za choonadi cha nkhani imene inali yosadziwika bwino poyifananiza ndi zinthu zimene anthuwo amazidziwa bwino. Iye analongosolera ndi kunena momveka bwino choonadi chozama ndi zithunzi zimene zinali zodziwika bwino monga mlimi wofesa mbeu kapena waulendo amene

amapita ku Yeriko (Msamariya Wachifundo). Zithunzi izi zinali za zinthu zomwe anthu a nthawiyo amazidziwa bwino ndipo kunali kosavuta kwa iwo kuti azimvetsetse ndi kuti zikhale za tanthauzo.

Mafanizo amakwana gawo limodzi la magawo atatu a ziphunzitsa za Khristu. Zambiri mwa nkhanizi zinali zophweka ndi zosavuta kumvetsetsa. Nthawi zambiri, mafanizo ake ngakhale kuti anali otambalala ndi osangalatsa, amanenedwa kuti apereke mfundo imodzi ya choonadi kapena uthenga. Khristu, amene anali mphunzitsi wamkulu, ndiye chitsanzo chimene tikuyenera kutengerapo mpaka lero. Kaphunzitsidwe aka kogwiritsa ntchito zifanifani ndi zinthu zochitika m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku motsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

Mafanizo a Khristu, amene ali osavuta kuwamvetsetsa ndi kuwambukira kusiyana ndi mau ozama onena za umulungu, amauluwula zambiri zokhudza Mulungu, chikhalidwe chake kapena onena za ufumu wa Mulungu mwa zina. Choonadi cha chiphunzitsa cha mpingo chikupezeka mu chophweka cha mafanizo. Chinyengo cha uchimo ndi kukhulukira kwa Atate zikunenedwa mozikizira mu nkhani yofunikira ya mwana wolowerera. Kufunikira kwa pemphero kukunenedwa mokumbutsana mu fanizo la mai wamasiye wosauka. Fanizo la anamwali khumi limatikumbutsa za kufunikira kokhala wokonzekera pamene tikuyembekezera kubweranso kwa mkwati. Nkhani ya nkhoa yosochera imaulula za chikhalidwe chokonda chimene ali nacho Mpulumutsi posakasaka otaika. Mafanizo okongola a Khristu ali miyala ya choonadi ya mtengo wapatali ndipo ali woyenera kuti tipitirize kuwaphunzira ndi kugawana ndi anthu ena. ■



“Yesu anaphunzitsa za choonadi cha nkhani imene inali yosadziwika bwino poyifananiza ndi zinthu zimene anthuwo amazidziwa bwino.”

Cholinga cha Mafanizo	Mau a Mkonzi	Mafanizo a Yesu	Zofunika pophunzira Mafanizo	Kodi Mukudziwa?
	Zogwiritsa ntchito polalikira		6-7	Mau a Nyengo Yake
2	3	4-5	Chithunzi cha Khristu	
			7	8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

Cholinga cha MAFANIZO

Yesu anagwiritsa ntchito mafanizo pofuna kuphunzitsa choonadi kapena kuyankha funso. Iye anagwiritsa ntchito zinthu zochitika m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku kuti anthu amene akumumvera amumvetse mosavuta. Katswiri wina wa malamulo anaimirira nafuna kumuyesa Yesu ndipo anafunsa kuti: "Ndipo mnansi wanga ndani?" (Luka 10:29). Yesu anapitiriza kulankhula ndipo ananena za nkhani ya Msamariya Wachifundo. Kenaka Yesu anafunsa kuti: "Uti wa awa atatu, uyesa iwe, anakhala mnansi wa iye uja adagwa m'manja a achifwamba?" (v. 36).

KUTULUTSA

KUWULULA

KUBISA

KUSUNGA

Yankho lake linali lodziwikiratu mu nkhanayi, komabe linapangitsa anthu omverawo kuti asinkhesinkhe ndi kulingalira paokha. Limawulula choonadi kuchokera kwa iwo amene akanatha kukana mau onenedwa mwachindunji.

Mafanizo a Khristu kawirikawiri amaulula choonadi mwa njira imene manenedwe ophweka

sangakwanitse. Iwo amene ali ndi mitima yoona mtima ndi yofunafuna adzamva ndi kumvetsetsa. Mafanizo amanenedwa ndi njira yofuna kupereka ndi kuulula choonadi mu njira yosavuta kumvetsetsa monga zilili mu chithunzithunzi chili m'mwambamu.

Mafanizo ena amene Yesu ananena analankhulidwa mu njira yakuti amafuna kubisa choonadi kwa iwo amene anasankha kuyenda mu mdima. "Ndipo ophunzirawo anadza, nati kwa Iye, Chifukwa chanji muphiphirsira iwo m'mafanizo? Ndipo Iye anayankha nati, Chifukwa kwapatsidwa kwa inu kudziwa zinsinsi za Ufumu wa Kumwamba, koma sikunapatsidwe kwa iwo. Pakuti yense amene ali nazo, kudzapatsidwa kwa iye, ndimo adzakhala nazo zochuluka; koma yense amene alibe, chingakhale chomwe ali nacho chidzachotsedwa kwa iye. Chifukwa chake ndiphiphirsira iwo m'mafanizo; chifukwa kuti akuona samaona, ndi akumva samamva, kapena samadziwitsa." (Mateyu 13:10-13). Munthu wosakhulupirira akhoza kukhala osamvetsetsa mfundo yaikulu ya fanizo, popeza zili zobisidwa kwa iwo amene "sakumva". Nthawi zambiri zimachitika kuti ophunzira aja amabwerera kwa Khristu ndi kumufunsa kuti anene mozama za tanthauzo la fanizolo.

Mafanizo anali osavuta kuwakumbukira chifukwa cha kulongosolera mwachifanifani ndipo ali othandiza pamene tikufuna kukumbukira choonadi cha uzimu. Iwo anali ndipo akadali ofunikira pofuna kusunga choonadi cha anthu ochokera ku zikhalidwe komanso malo osiyanasiyana. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, monga anakhoza kumva; ndipo sanalankhule nao wopanda fanizo: koma m'tseri anatanthauzira zonse kwa ophunzira ake. —Marko 4:33-34

Kalata ya Gospel Truth ya ulendo uno ikutsindika za mafanizo a Yesu. Mafanizo anali gawo lofunikira la ziphunzitso za Khristu, ndipo ngakhale lero lino ali ndi chuma chopindulitsa pa ziphunzitso zathu za masiku ano. Mafanizo amalongsola choonadi mu njira zimene mfundo sizingakwanitse kutero. Ngakhale kuti ziphunzitso za Khristu zongofuna kuonetsera, komabe Iye analankhula ku zinthu zimene zimakhudza moyo wao mwa njira yosavuta kumvetsa. Akatswiri a Baibulo ndi iwo amene anazama nalo Baibulo nthawi zina samvana chimodzi za tanthauzo la fanizo komanso chimene chimapanga nkhani kuti ikhale fanizo kusiyana ndi ina imene ili ngati nthano chabe. Fanizo lenileni ndi nkhani yokhala ndi choonadi chobisika imene imafananiza chinthu chochitika tsiku ndi tsiku pakati pathu ndi tanthauzo lauzimu.

Mtolo wanga ulendo uno ndi wakuti ndiwalimbikitse anthu kuphunzira mafanizo ndi kuti adzimize wokha mu chiphunzitso chodabwitsa cha Khristu chimene chimakhala ndi zithunzi zofotokozera. Aliyense amaphunzira mosiyanasiyana, ndipo Khristu anaona kuti kunali kofunikira kuti awafikire anthu ndi nthano komanso zitsanzo kuti iwowo akhoza kuchilandira choonadi mosavuta.

Zaka zingapo zapitazo, ndinali ndi mwai wopangitsa maphunziro a atumiki a Mulungu kwa masiku angapo ndi gulu lina ku Africa. Poyamba mu nthawi zokhala ngati zomwezi, timaphunzirira limodzi maphunziro ena ndi ziphunzitso za mpingo. Koma panthawiyi ndinaona kuti tichite zinthu mosiyana. Mulungu anandiululira mphamvu ya mafanizo. Maso anga anatsekuka ku zodabwitsa za choonadi zimene zipezeka mu mafanizo a Khristu. Kwa masiku angapo, atumiki a Mulungu anaphunzira zokhudza mafanizo ndipo anagawana limodzi zimene anatolapo. Ndinadalitsika kwambiri kuti ndinatha kupereka maphunziro othandiza pamapeto a phunziro lililonse pamene tinakambirana za mitu yosiyanasiyana monga: pemphero, kukhulukira, chipulumutso, chikondi cha Mulungu, chiweruzo, uchimo, Ufumu wa Mulungu, chifundo, moyo wamuyaya, kumwamba, gehena, kufalitsa uthenga wabwino ndi zina zambiri. Pali choonadi komanso ziphunzitso za mpingo zimene zimapezeka mu nkhani zimenezi, ndipo zimawafikira anthu mu njira imene mphunzitsi wongoyima ndi kumauza ana zoyenera kuchita sangafikirepo.

Pemphero langa ndilo lakuti Mulungu akutakasani kuti muwerenge mafanizo ndi kuzindikira chuma komanso mphamvu zimene zabisika m'menemo.

Michael W. Smith

July 2021



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Zogwiritsa ntchito polalikira



Nkhani zokhala ndi zifanifani ndiponso za zinthu zomwe zinachitikadi zili zopindulitsa pofuna kunena choonadi kwa iwo amene akumvera. Nkhani zokhala ndi zifanifani zikhoza kuwapangitsa anthu kuti aimvetsetse komanso kuchipanga choonadi kuti chikhale chofunikira mu masiku athu ano ndi zikhalidwe zathu. Komabe, pamene tikukambirana nkhani kuti tifikire pa mfundo inayake, chimenechi chikhoza kukhala chida chofunikira kwa wolalikira, ndipo mtumiki wa Khristu sakuyenera kukhala munthu wongosangalatsa anthu kapena wazisudzo. Ntchito yathu ndiyo ya kulalikira Mau a Mulungu. Ngati nkhani ili

yothandiza, tikhoza kuigwiritsa ntchito, koma tisalole kuti kukamba nkhani kusatenge malo a choonadi chenichenicho.


Nkofunikanso kuti pamene tikufotokozera za chithunzi tiyesetse kuti tisachipangitse kuti chikhale choonadi chifukwa mukufuna chigwirizane ndi chitsanzo chanu kapena nkhani yanu. Alaliki ambiri pogwiritsa ntchito zinthunzi alakwitsa ndipo potero udindo wa choonadi ndi chithunzi wabwezedwa. Chinachake ndi choonadi popeza ndi Mau a Mulungu, osati chifukwa tikunena nkhani imene tikhoza kupezamo choonadi. ■

Mafanizo a Yesu

“Ndipo Iye anawaphera fanizo nanena...”

Fanizo	Mateyu	Marko	Luka
Ufumu wa kumwamba			
Wofesa	13:3-8, 18-23	4:4-8, 14-21	8:5-8, 11-15
Kambewu ka mpiru	13:31-32	4:30-32	13:18-19
Chotupitsira mkate	13:33		13:20-21
Chuma chobisika	13:44		
Mwala wa ngale	13:45-46		
Mbewu		4:26-29	
Kutaika ndi Kubwezeretsedwa			
Nkhosa yosochera	18:10-14		15:1-7
Ndalama yotaika			15:8-10
Mwana wolowerera			15:11-32
Kumvera/Kusamvera			
Nyumba yomanga pathanthwe	7:24-27		6:47-49
Anyamata awiri	21:28-32		
Akapolo osapindulitsa			17:7-10
Kutumikira			
Matalente	25:14-30		
Kapitao wochenjera			16:1-13
Ndalama khumi			19:11-27
Khristu			
Antchito oipa	21:33-45	12:1-12	20:9-19

Nkhosa



Wofesa ndi Mbeu

Fanizo	Mateyu	Marko	Luka
Pemphero			
Bwenzi laliuma			11:5-13
Woweruza wosalungama			18:1-8
Mfarisi ndi wokhometsa msonkho			18:9-14
Chikondi ndi Utumiki			
Msamariya wachifundo			10:30-37
Kukhululuka			
Kapolo wopanda chifundo	18:21-35		
Angongole awiri			7:41-43
Za masiku otsiriza/Kukonzekera			
Nansongole	13:24-30, 36-43		
Khoka	13:47-50		
Antchito olembedwa mwina mwina	20:1-16		
Phwando la ukwati	22:1-14		
Mwini chuma wopusa			12:16-21
Za Kudikira		13:34-37	12:35-40
Akapolo awiri	24:45-51		12:42-48
Anamwali khumi	25:1-13		
Mkuyu wosabala			13:6-9
Phwando lalikulu			14:15-24



Mwana wolowerera

Nkhani ndi zifanifani zingapo



Ndalama yotaika

Nkhani/Chithunzi	Mateyu	Marko	Luka
Mchere wa dziko lapansi	5:13	9:50	14:34-35
Kuunika kwa dziko	5:14-16	4:21-22	8:16-18
Diso ndi dzanja lochimwitsa	5:29-30; 18:8-9	9:43-47	
Chuma cha m'mwamba	6:19-21		
Makwangwala ndi maluwa	6:25-34		12:22-32
Kachitsotso ndi chimtanda	7:1-5		6:41-42
Zipata ziwiri	7:13-14		
Ngamila/Diso la singano	19:23-24	10:23-25	18:24-25
Chikho ndi mbale	23:25-26		11:37-39
Nkhosa ndi mbuzi	25:31-46		
Mipando yaulemu			14:7-14
Kumanga nsanja/ Kupita kunkhondo			14:25-33
Mwini chuma ndi Lazaro waumphawi			16:19-31
Mbusa wabwino	Yohane 10:1-16		

ZOFUNIKA POPHUNZIRA MAFANIZO



Matalente

“Kumasulira kwa fanizo kudzikhala kogwirizana ndi zina zonse zimene zili m’malemba komanso ziphunzitso za Khristu ndi Atumwi.”

Kuphunzira mafanizo ndi chinthu chosangalatsa ndipo ndi njira yabwino pofuna kuphunzira zambiri mwa ziphunzitso za Khristu. Iwo ndi oposa nkhani chabe, ndipo ndi zipangizo zogwirika zothandiza kuti tizindikire zoonadi zozama za ziphunzitso. Cholinga chenicheni cha choonadi chimene chili mu fanizo sichidzatsutsana ndi ziphunzitso zina za m’malemba, koma kuti malemba ndi mauneneri ena amene ali ovuta kuwamvetsetsa akuyenera kutanthauziridwa kuti agwirizane ndi ziphunzitso za Khristu zimene zinali zosavuta kuzimvetsa. Nkofunikira kwambiri kuwawunguza mafanizo moona mtima komanso ndi kufunitsitsa kwakuti timvetsetse kwambiri tanthauzo lawo lenileni. Mfundo zimene zili m’munsimu zikhoza kuthandizira kuti tione zimene tingachite pofuna kuti tikwanitse kuwamvetsetsa mafanizo odabwitsa a Yesu Khristu.

Lingalirani za malo amene ndimeyo ikupezeka mu Baibulo

Phunzirani za pamene fanizolo likupezeka. Fufuzani zimene zikunenedwa kumbuyo ndi kutsogolo kwa fanizolo. Nthawi zambiri, Yesu amanena momveka bwino za cholinga kapena tanthauzo limene iye anapereka. Fanizo la mzimai wamasiye ndi woweruka wosalungama mu Luka 18:2-6 likhoza kutanthauzira molakwika ngati sitilabadira za malo amene likupezeka mu baibulo. Munthu atangomva akhoza kungoganiza nkhanayi ikunena kuti Mulungu ndi wosalungama komanso wosasalira. Komatu imeneyi si mfundo imene fanizolo likunena, iyayi, Yesu ananena za cholinga chake mu vesi yoyamba imene ikuti, “Ndipo anawanenera fanizo lakuti ayenera iwo kupemphera nthawi zonse, osafooka mtima.”

Fufuzani mfundo zonse bwino lomwe

Mafanizo ena ali ndi zinthu zina zambiri zimene zilibe tanthauzo lauzimu lenileni. Zinazo zimanenedwa pofuna kukometsera nkhanayo ndi kupereka chithunzi chimene chikubwera pamwamba pa choonadi chاوزimu. Fanizo la woweruka wosalungama silikunena kwambiri za Mulungu koma kuti zochitika mu nkhanizo zikufuna kuonetsera mtima wokakamira ndi kusatopa kwa mai wamasiye uja. Samalani popeza simukuyenera kupereka tanthauzo lauzimu ku china chilichonse chimene chikupezeka mu fanizo.

Kunanenedwa kuti “fanizo silinayikidwe kuti litanthauzire kenakalikonse.” Si chilichonse chimene chili phunziro kapena chofanizira. Chifukwa cha ichi, si nthawi zonse pamene mafanizo amakhala ndi phunziro, monga momwe si chilichonse chimene chili ndi

tanthauzo lauzimu. Tikafuna kuti tipeze tanthauzo pa kena kalikonse tidzasemphana ndi tanthauzo lenileni la fanizolo.

Khalani ndi chidwi ndi zinthu zimene zikubwerezedwa

Kawirikawiri Yesu anagwiritsa ntchito zinthunzi zimene zimabwerezedwa mu Malemba ndipo zili ndi matanthauzo ofanana kuchoka pa fanizo kupita pa fanizo linzake. Nthawi zambiri, mbuye, woweruka kapena mfumu zimaimira mfumu. Nkhosa zimaimira ana a Mulungu, ndipo mbuzi zimaimira anthu osaombedwa. Mbusa, woyang’anira munda, kapena mwana wa mfumu nthawi zambiri amaimira Khristu.

Kodi chinachitsa ndi chiyani kuti Fanizo linenedwe?

Pamene Yesu amanena mafanizo, nthawi zina amayankha funso kapena kunenapo za chikhalidwe china chimene amachita anthu amene anali pamenepo. Mu Luka 15, Yesu ananena mafanizo a nkhoa yosochera, ndalama yotaika, ndiponso mwana wolowerera. Yesu ananena mafanizo awa pofuna kuyankha Afarisi ndi Alembi amene amang’ung’udza ndi kumanena kuti, “Uyu alandira anthu ochimwa,



Akapolo ogwira ntchito m’munda

nadya nao (v. 2).” Kumvetsetsa chimene chinapangitsa kuti mafanizo linedwe zimathandizira kuti munthu adziwe cholinga cha mafanizo. Mu nkhani iyi, amafuna kuonetsera mmene Mulungu amawaonera anthu ochimwa.

Yang’anani mfundo imodzi yaikulu

Mafanizo amanenedwa kuti atsindike mfundo inayake. Pamene mukuwerenga, muzukute mosamalitsa choonadi chenicheni chimene Yesu akuchinena ndipo musaiwale kumene nkhaniyo yachokera ngakhale cholinga chimene chinamupangitsa Yesu kuti ayinene nkhaniyi. Pofuna kuti tithandizane kuti tilunjike pandunji pa nkhani, taganizani za mayankho ku mafunso awa:

1. Kodi ndi ziti zimene zikusiyana zomwe zikupezeke mu fanizo?
2. Kodi ndi ndani amene akutenga gawo lalikulu?
3. Kodi ndi ndani kapena chiyani chimene fanizolo likukhazikikapo?
4. Kodi chinachitika ndi chiyani kumapeto kwa fanizolo?

Phunzirani chikhalidwe ndi mbiri ya anthuwo

Kuti tiwamvetsetse bwino mafanizo tikuyenera kuti timvetse mbiri ndi chikhalidwe cha anthu amene akunenedwa mu fanizolo. Mafanizo ena amakamba za chinthu chinachake kapena mwambo wina wake umene Ayuda a nthawi imeneyo ankaumvetsa bwino. Chitsanzo ndi fanizo la phwando la ukwati pa Mateyu 22:1-14. Munthu amene analibe zovala za ukwati anaponyedwa kumtima wakunja. Munthu wina akhoza kumumvera chisoni munthu amene sanathe kuvala zovala zoyenerera, mpaka pamene wazindikira kuti panthawi imene Yesu ankalankhula fanizolo, unali mwambo wakuti mwini ukwati amapereka zovala zoyenerera kwa alendo amene abwera ku ukwati wake. Zimene zikutanthauza kuti munthuyu anachita kusankha kuti asavale chimene anapatsidwacho. Zikaterere munthu tsopano umatha kumvetsetsa choonadi cha chiphunzitsotso chokhudza gehena komanso chilango.

Kumasulira

Kumasulira kwa fanizo kudzikhala kogwirizana ndi zina zonse zimene zili m’malemba komanso ziphunzitsotso za Khristu ndi Atumwi. Ngakhale kuti tikhoza kupeza choonadi kuchokera ku nkhani inayake, wowerenga asamalitse kuti asapange chiphunzitsotso kuchokera ku kumasulira kolakwika kwa fanizo. Fanizo limafananiza pakati pa zinthu ziwiri. Ngati fanizolo ndi lokhudza za ufumu wa Mulungu, kumasulira kwake kukhala kokhudzana ndi ufumu wa Mulungu, osati mmene nkhaniyo ikugwirizanirana ndi zinthu zokhudza banja, zandale ndi zina zotero. Kumbukirani kuti maganizo ambiri amakhala ndi tanthauzo limodzi.



Anamwali Khumi

Kuyambira kalekale, anthu akhala akupereka matanthauzo opeka kapena kunena mau ophiphiritsa ku mafanizo ena. Nthawi zambiri izi zimatsutsana ndi zimene zakambidwa kapena cholinga cha fanizolo. Martin Luther anawatchula mamasulidwe ophiphiritsa a mafanizo kuti anali “chozwizwitsa chopanda pake” ndipo “zinthu zopindulitsa.”

Fufuzani ndipo mugwiritse ntchito

Pamene fanizo lawerengedwa ndi kuwunikiridwa kuti tipeze kumasulira kwenikweni, nkofunika kuti ifeyo tichigwiritsa ntchito chiphunzitsotso. Kodi zimenezi zikundiphunzitsa chiyani zokhudzana ndi ufumu wa Mulungu komanso zinthu zimene zili nkudza? Nanga choonadi chimenechi moyo wanga ungapindule nacho bwanji? Kodi Mulungu akufuna kuti ndichite chiyani?

Kuphunzira mafanizo kudzabweretsa madalitso, zobetchera komanso chilimbikitso kwa owerenga. Tiyeni tifunefune kuti tidziwe, tiphunzitse kuti timvetsetse, ndipo tikhumbwe kumudziwa Mulungu kuti potero tipezeke kukhala okhulupirika pa kubweranso kwa Ambuye. ■

Chiithunzi cha Khristu

Uthenga Wabwino wa Yohane umakhazikika pa kutipatsa chithunzi chenicheni cha Yesu, makamaka chikhalidwe chake ndi zimene amachita. Pali zifanifani zokwana 9 mu Yohane zimene zikugwiritsidwa ntchito pofuna kunena za Yesu.

1. INE NDINE mkate wopatsa moyo/Mkate Wamoyo—Yohane 6:35, 48, 51.
2. INE NDINE kuunika kwa dziko lapansi—Yohane 8:12; 9:5.
3. Abrahamu asanakhalepo, INE NDINE—Yohane 8:58.
4. INE NDINE khomo—Yohane 10:7, 9.
5. INE NDINE mbusa wabwino—Yohane 10:11, 14.
6. INE NDINE kuuka ndi moyo—Yohane 11:25.
7. INE NDINE Njira, Choonadi ndi Moyo—Yohane 14:6.
8. INE NDINE Mpesa weniweni—Yohane 15:1, 5.
9. INE NDINE Iyeyo—Yohane 18:5-6.





KODI MUKUDZIWA?

Ambiri mwa mafanizo a Khristu akupezeka mu mauthenga abwino atatu oyamba amene amalemba mofanana (Mateyu, Marko, ndi Luka). Pamene Uthenga wabwino wa Yohane uli ndi nkhani zochepa ndiponso zithunzithunzi zomwe sizili mafanizo enieni. Pa Yohane 10:6 akugwiritsa ntchito mau akuti “fanizo”, komabe ndi mau ena a chigriki amene ali osiyana ndi mafanizo ena ndipo amanena za chithunzithunzi kapena chifanizo cha mau.



MWALA WA NGALE WA MTENGO WAPATALI

Ndiponso Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi munthu wa malonda, wakufuna ngale zabwino: ndipo m'mene anaipeza ngale imodzi ya mtengo wapatali, anapita, nagulitsa zonse anali nazo, naigula imeneyo.

—Mateyu 13:45-46

Cholinga cha munthu wamalonda ndicho kugula ndi kugulitsa malonda pofuna kuti apeze phindu lochuluka. Kwa zaka zankhaninkhani, anthu akhala akuika miyoyo yawo pachiswe ndipo akhala akuwoloka nyanja zazikulu ndipo akafika ku maiko achilendo chifukwa chofuna chuma ndi kulemera. Mavuto ndi zoopsa zimene anakumana nazo paulendo zinaoneka kuti zinapindula powerengera zimene anaononga ndi chuma cha padziko lino chimene angachipeze atabwerako ku ulendoko.



Yesu analankhula fanizoli pofuna kupereka chithunzi cha kupulumutsidwa ku uchimo ndipo mphoto yamuyaya ikutengedwa ngati mwala wa mtengo wapatali kwambiri. Munthu wamalonda, pamene wapeza mwala wantengo wapatali kwambiri, amagulitsa katundu wake yense pofuna kuti agule chinachake chimene chili cha phindu lalikulu. Chipulumutso ndi cha mtengo wake woposa mwala uliwonse umene tingaganizire. Munthu amene akufuna chipulumutso mwachimwemwe ndi mokondwera akuyenera kusiya zonse za dziko lino lapansi pamene nafunafuna Khristu komanso kuombedwa ku machimo. Mwala uwu wa mtengo wapatali ukhoza ndipo ungapezedwe ndi okhawo amene akuwufunafunana ndi mitima yawo yonse.

Akhristu amene ali aulesi ndi osakhazikiza pa machitachita awo ndi Mulungu ndiye kuti sanapulumsidwe zenizeni kapena ali mu chiopsezo chakuti akhoza kutaya izo zimene ali nazo. Pofuna kutsata Yesu, tikuyenera kusiya zonse kuti mwakutero tipeze mphamvu ndi chimwemwe cha chipulumutso chenicheni. Tikuyenera kufunafuna icho chimene mwana wa ngale wantengowapatali ndi mtima wathu wonse, ndipo pasakhale chotibweza m'mbuyo.

Pamene tipeza mwala wa mtengo wapatali, chipulumutso ku uchimo ndiponso chiyembekezo cha moyo wosatha, zidzitsogozedwa ndi mtendere wamumtima komanso chimwemwe chimene dziko lino silinangapereke. Pokhala atumiki a Ambuye, tikuyenera kupereka uthenga wa choonadi chenicheni ndiponso phindu la chipulumutso. Miyoyo yathu ikhale chitsanzo cha chuma ndi chimwemwe cha chipulumutso chathunthu. Mdaniyo amafuna kutipangitsa ife kuti tipereke chithunzi choipa chokhudzana ndi kugulitsa zinthu zina zonse kusiyana ndi kuyang'anitsitsa pa chuma cha mtengo wapatali chimene chipezeka mwa Yesu Khristu.

Ngati muli opulumutsidwa ndipo mumamudziwa Yesu Khristu, muli ndi mwala wangale wa mtengo wapatali. Pitani mukawuze munthu wina za chipulumutso chachikuluchi kuti nawonso akhoza kukhala ndi moyo wosatha. ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE